# ALIMI ALI NDI NJIRA ZINA M'MALO

## MWA NDONDOMEKO ZA KUKWEZA NTCHITO ZA MALIMIDWE (GREEN REVOLUTION)

Akatswiri ambiri a zaulimi akhala akunena kuti palibe luso limodzi limene lingasinthe nthito za ulimi za mu Africa. M'malo mwake, amanenetsa kuti alimi azigwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana zochokela ku ndondomeko zosiyanasiyana za malimidwe.

Ngati mlowa m'malo wa ndondomeko za makamphani zodzala mtundu umodzi wa mbeu, njira za ulimi wosamala za chilengedwe zimalimbikitsa umoyo wa m'nthaka komanso chonde, ndondomeko zokhazikika za kalimidwe ka chakudya komanso kuchulukitsa cholowa cha pakhomo pa alimi.

- Tsala – kusiya munda osalimidwa kuti chonde chibwelela kwa kanthawi;
- nkhuti za manyowa komanso kompositi;
- kuchulukitsa zinyalala zowonelana – kuwonjezelapo dothi la pachulu, manyowa a ziweto ndi masamba amene akuwola;
- kasakaniza wa mbeu za mgulu la njere ndi za mgulu la nyemba, monga khobwe komanso nzama;
- kubwezela mchere wa nitrogen;
- kasinthasintha wa mbeu – mwa chitsanzo, za mgulu la njere, mtedza komanso mitengo ya mgulu la nyemba (Msangu);
- ulimi wophatikiza mitengo – kasakaniza wa mitengo, mbeu komanso ziweto;
- chulukechuluke wa mitundu ya mbeu komanso ndondomeko za mbeu zoyendetsedwa ndi alimi zothandizidwa bwino.

Njira za malimidwe zosamala chilengedwe zimene zilipo pano zinayikika pa malimidwe a makolo zimene zakhala zikusulidwa kwa zaka mazanamazama ndi alimi akuno ku Africa. Machitachita amenewa ndi awo a alimi, amene ayenela kuyikidwa nawo mu kafukufuku komanso ntchito zachitukuko zimene zimawakhudza.

duducoelho.com

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156

african centre for biodiversity